

MATENDA AMENE

KAWIRIKAWIRI SITIWAMVETSA

2

Kodi chimayambitsa matenda ndi chiyani?

Anthu am'madera osiyanasiyana komanso ogwira ntchito zosiyanasiyana amafotokoza mosiyanasiyana pa zomwe zimayambitsa matenda.

Mwana akatsekula m'mimba: Kodi chifukwa chiyani?

Anthu akumudzi amanena kuti makolo anachita chinthu china cholakwika kapena kuti akwiyitsa mizimu.

Dokotala atha kufotokoza kuti mwina mwanayo m'thupi mwake mwalowa tizilombo toyambitsa matenda.

Wogwira ntchito zaumoyo atha kunena kuti anthu a m'mudzimo alibe madzi abwino komanso mwina sagwiritsira ntchito zimbudzi.



Wogwira ntchito zolimbikitsa kusintha zinthu pakati pa anthu anganene kuti kusowa ukhondo komwe kumayambitsa kutsekula pakati pa ana kumadza chifukwa chosowa chilungamo pakagawidwe ka malo ndi chuma.

Mphunzitsi atha kunena kuti kutsekula kwa m'mimba kumadza chifukwa cha kusaphunzira.

Zomwe zimayambitsa matenda zimafotokozeredwa mosiyanasiyana malinga ndi momwe aliyense akudziwira. Nanga wolondola ndani? Mwina aliyense ndi wolondola kapena ndi wolondola pang'ono. Izi zili chomwechi chifukwa. . .

Matenda amayamba pa zifukwa zosiyanasiyana.



"Chifukwa ninji mwana wanga?"

Chifukwa chilichonse chomwe chaperekedwa pamwambapa chikhoza kukhala chimodzi mwa zifukwa zoyambitsa kutsekula m'mimba.

Pofuna kupewa ndi kuchiza matenda ndi bwino kudziwa matenda opezeka m'dera lanulo ndi kudziwanso zomwe zimayambitsa matendawo.

Mu buku lino takamba za matenda osiyanasiyana malinga ndi mankhwala a makono.

Kuti mupindule ndi bukuli ndi kugwiritsira ntchito bwino mankhwala amene tavomereza ndi kofunika kumvetisa za matenda ndi chomwe chimawayambitsa molingana ndi njira zamakono za sayansi. Kuwerenga mutu uno kutha kuthandiza.

Matenda osiyanasiyana ndi zomwe zimayambitsa

Matenda angagawidwe m'magulu awiri motere: Matenda opatsirana ndi matenda osapatsirana.

Matenda opatsirana: Awa ndi matenda omwe angafale kuchokera kwa munthu wina kupita kwa winanso. Anthu amene sakudwala ayenera kutetezedwa kwa omwe akudwala.

Matenda osapatsirana: Awa ndi matenda omwe safala kuchokera kwa munthu wina kupita kwa wina. Matendawa amayamba pa zifukwa zina. Choncho ndi kofunika kudziwa matenda omwe ndi opatsirana komanso omwe ndi osapatsirana.

Matenda osapatsirana

Zoyambitsa matendawa ndi zambiri koma sayamba chifukwa cha majeremusi, bakiteriya kapena tizilombo tina. Matendawa safala kuchoka kwa munthu wina kupita kwa wina. Choti tidziwe ndi chakuti mankhwala onse omwe ali olimbana ndi tizilombo toyambitsa matenda sathandiza kuchiza matendawa (onani tsamba 56).

Kumbukirani: Mankhwala olimbana ndi tizilombo toyambitsa matenda sathandiza pa matenda osapatsirana.

ZITSANZO ZA MATENDA OSAPATSIRANA

<p>Matenda amene amayamba chifukwa cha kuwonongeka kwa ziwalo kapena zovuta zina m'thupi:</p> <ul style="list-style-type: none"> • nyamakazi • matenda a mtima • linjirinjiri • kufa kwa ziwalo • mutu wa ching'alang'ala • matenda a maso (ng'ala) • khansa (<i>cancer</i>) 	<p>Matenda amene amayamba ndi zinthu zakunja zomwe zimawononga thupi:</p> <ul style="list-style-type: none"> • ziwengo (<i>allergies</i>) • mphumu • kumwa/kudya poyizoni • kulumidwa ndi njoka • chifuwa chifukwa chakusuta • zilonda zam'mimba • uchidakwa 	<p>Matenda amene amayamba chifukwa cha kusowa kwa zinthu m'thupi:</p> <ul style="list-style-type: none"> • kunyentchera • kuchepa kwa vitamin B • kuchepa kwa magazi • chithokomiro/nkhwiko (<i>goitre</i>) • matenda a chiwindi • kusawonetsetsa
<p>Matenda obadwa nawo:</p> <ul style="list-style-type: none"> • nthenda ya mlomo wogawika (<i>harelip</i>) • nthenda ya maso oyang'ana chambali • linjirinjiri (khunyu) • ana opepera • zipsera za chibadwa • maso ntchefu 	<p>Matenda oyamba chifukwa cha maganizo:</p> <ul style="list-style-type: none"> • mantha ndi zinthu zosadziwika bwino • kukhala wodandaula 	


Matenda opatsirana

Matenda amayamba ndi tizilombo tating'onoting'ono tomwe timaononga thupi. Matendawa amafala m'njira zambiri. Zitsanzo za tizilombo toyambitsa matenda ndi izi:

ZITSANZO ZA MATENDA OPATSIRANA

Choyambitsa matenda	Nthenda yake	Kafalidwe/m'mene imalowera m'thupi	Mankhwalwa ake
bakiteriya (majeremusi)	TB	kudzera mu mpweya (kutsokomola)	mankhwalwa osiyanasiyana opha bakiteriya kapena majeremusi
	kafumbata	mabala osatsuka	
	kutsekula m'mimba	zala zosatsuka, madzi, ntchentche	
	chibayo chamitundu yosinasiyana	kudzera mu mpweya (kutsokomola)	
	chinzonono, mabomu ndi chindoko	kugonana	
	kupweteka kwa mkhutu	chimfine ndi zilonda zakukhosi	
	zilonda	kukhudza zinthu zonyansa	
	zilonda zamafinya	kukhudzana	
vayirasi (majeremusi)	chimfine, kuphwanya kwa thupi, chikuku, kufa ziwalo kwa ana, kutsekula m'mimba, masagwidi, katsabola, mavairasi	kuchokera kwa wodwala wina, kudzera mu mpweya, kutsokomola, ntchentche	<i>Aspirin</i> ndi mankhwalwa ena ochepetsa ululu (palibe mankhwalwa omwe amathana ndi mavairasi kotheratu). Katemera amathandizanso kulimbana ndi matenda a mavairasi.
	chiwewe	kulumidwa ndi nyama	
	njerewere	kukhudzana	
fangasi (<i>fungus</i>)	chipere	kukhudzana kapena kubwerekana zowala	<i>sulfur</i> ndi <i>vinegar undecylenic, benzoic, salicylic acid, griseofulvin</i>
	linyetsu		
tizilombo tokhala m'kati mwa thupi	M'matumbo njoka zam'mimba (kutsekula m'mimba)	kamwa kokhudzana ndi chimbudzi uve	mankhwalwa osiyanasiyana
	m'magazi: malungo	udzudzu	<i>chloroquine</i> ndi mankhwalwa ena a malungo
tizilombo tokhala pa thupi	nsabwe	kukhudzana ndi anthuodwala kapena zovala zawo	mankhwalwa opha tizilombo, <i>lindane</i>
	utitiri		
	nsikidzi		
	mphere		

Bakiteriya monganso tizilombo tina tomwe timayambitsa matenda ndi wochepa kwambiri moti sangawoneke popanda makina otchedwa *microscope* – awa ndi makina amene amakulitsa tinthu tating'ono kwambiri. Mavairasi ndi ochepa kwambiri kuposa bakiteriya.



Matenda oyamba chifukwa cha bakiteriya angachizidwe ndi mankhwalwa opha tizilomboti monga penicillin (*penicillin*) ndi *tetracycline*, mankhwalawa sachiritsa matenda oyamba ndi Mavairasi monga chimfine, kuphwanya kwa m'thupi, masagwidi, katsabola ndi matenda ena. **Matenda oyamba chifukwa cha mavairasi sangachizidwe ndi mankhwalwa ochiza matenda oyamba chifukwa cha bakiteriya.** Sangathandize ndipo angakhale mankhwalwa owopisa (onani tsamba 58).

Matenda ovuta kusiyanita

Nthawi zina matenda omwe amayamba mosiyana ndipo osoweka mankhwala osiyana amadzetsa mavuto omwe amawoneka ofanana. Mwachitsanzo:


1. Mwana amene akuwonda pang'onopang'ono kwinku mimba yake ikutupa atha kukhala ndi limodzi mwa mavuto awa:

- kuperewera kwa zakudya m'thupi (onani tsamba 117)
- njoka zam'mimba – tsamba 146 (zimagwirizana ndi kuperewera kwa zakudya m'thupi)
- TB ya m'mimba (onani masamba 189-190)
- matenda a m'chikhodzodzo (onani tsamba 244)
- matenda a chiwindi kapena kapamba
- khansa ya m'magazi



2. Munthu wamkulu amene ali ndi bala lomwe likukulirakulira pamwendo atha kukhala ndi mavuto awa:

- kusayenda bwino kwa magazi m'thupi (onani tsamba 225)
- nthenda ya shuga (tsamba 132)
- nthenda ya mafupa (*osteomyelitis*)
- khate (onani tsamba 199)
- TB ya pakhungu (onani tsamba 224)
- chindoko (onani tsamba 253)



Alionse mwa matenda omwe atchulidwawa ali ndi mankhwala ake, choncho ndi kofunika kuwasiyanita molondola.

Matenda ambiri poyamba amawoneka ofanana koma mukafunsa bwinobwino ndikudziwa chomwe mukufuna, mutha kuwona zizindikiro zokudziwitsani chenicheni chomwe munthuwo akudwala.

Bukuli likufotokoza chiyambi ndi zizindikiro za matenda ambiri. Komatu ndi pofunika kusamala! Matenda si kuti nthawi zonse amaonetsa zizindikiro zomwe zatchulidwazi. Mwinanso zizindikirozi zimakhala zozunguza. **Pa matenda ovuta munthu wodziwa ntchito zachipatala kapena dokotala ndiye angathe kuthandiza.** Nthawi zina pamafunika kupima munthu yemwe akudwalayo mwapadera.

Muchite zomwe mungathe!!!
Pogwiritsira ntchito bukuli, kumbukirani kuti ndi kosavuta kulakwitsa.
Musasonyeze ngati kuti mumadziwa zinthu zomwe simukuzidziwa.
Ngati simukudziwa bwino za matenda ena ake ndi momwe
mungawachizire, kapena ngati matendawa ndi aakulu,
pitani ku chipatala.

Matenda omwe anthu amawasokoneza kapena kuwapatsa mayina ofanana

Mayina ambiri amene anthu amagwiritsira ntchito pa matenda osiyanasiyana ankagwiritsidwa ntchito anthu asanadziwe za majeremusi kapena bakiteriya ndipo anali asanadziwense mankhwala ochiza matendawo. Matenda ambiri amene anali ndi mavuto ofanana monga kutentha thupi ankapatsidwa dzina limodzi. M'mayiko ambiri mayina ofananawa akugwiritsidwabe ntchito. Madokotala omwe aphunzira ntchitoyi kumadera a ku matauni sadziwa za maina amenewa ndipo sawagwiritsira ntchito. Pa chifukwa chimechi anthu amaganiza kuti madokotalawo sangathe kuchiza matendawo ndipo **amayesera kuchiza matendawo** pogwiritsira ntchito mankhwala azitsamba.

Matenda amene amadziwika ndi mayina a kumudziwa ndi omwewo amene amadziwikanso ndi mayina amakono asayansi. Kusiyanana kwake kwagona pa mayinawo basi.

Pa matenda ambiri, machiritso a pakhomu amagwira bwino ntchito. Koma pali matenda ena oyenera kuchizidwa ndi mankhwala amakono pofuna kuteteza moyo makamaka pa matenda owopsa monga chibayo, taifodi, TB, kapena zovuta zomwe zimadza kwa mayi akabereka mwana.

Pofuna kudziwa matenda oyenera kuchizidwa ndi mankhwala amakono ndi mtundu wa mankhwala ake ndi kofunika kuti **mudziwe za nthendayo malinga ndi momwe anthu achipatala adaphunzirira komanso malinga ndi zomwe zili m'buku lino.**

Ngati simupeza matenda amene mukufuna m'buku lino, fufuzani pamene pali matenda ofanana nawo pogwiritsa ntchito dzina lina la nthendayo kapena pa mutu womwe ukunena za vuto limeneli. Werengani NDONDOMEKO YA MITU koyambirira kwa bukuli.

Ngati simukutha kuzindikira bwino za matenda makamakanso ngati ali owopsa, pitani kuchipatala.

Mutu uno ukupereka zitsanzo za matenda amene ali ndi mayina a kumudzi. Nthawi zambiri dzina limodzi limaperekedwa ku matenda osiyana malinga ndi kafukufuku wa mankhwala amakono.

Sikungatheke kupereka zitsanzo za dziko lililonse kapena dera lililonse komwe bukuli lingagwiritsidwe ntchito. Zitsanzo za mayina omwe aperekedwa sizingakhale zomwe inu mukudziwa. Komabe anthu kulikonse pa dziko lapansi amakamba za matenda awo mofanana. Choncho zitsanzozizi zingakuthandizeni kuganiza momwe anthu amatchulira mayina ku dera lanu.


Kutentha kulikonse kwa thupi nthawi zambiri kumatchedwa malungo ngakhale kuti kutha kukhala matenda ena. Nthenda ya chikasu nthawi zambiri imatchedwa 'yellow fever'. Pakati pa mtundu wa a Yoruba kuzambwe kwa Africa, nthenda iliyonse ya m'mimba imatchedwa 'arun'. Vuto lililonse lokhudza kuthako chifukwa cha zilonda kapena kunyerenyesa limatchedwa 'gedegede'. Timadontho tonga khungu la kambuku pamwendo timatchedwa 'inarun' kutanthauza kuti 'moto wochokera kumwamba'.

Kodi matenda otsatirawa amatchedwa chiyani kudera lanu? Ngati mukudziwa lembani dzinalo pamene palembedwa kuti:

Dzina la kudera la kwanu: _____

Zitsanzo za mayina amatenda m'madera osiyanasiyana

KUTSEKA KWA MATUMBO Dzina la kudera la kwanu: _____



Matenda aliwonse oyambitsa kupweteka kwa m'mimba kapena kutsekula kwa m'mimba amatchedwa **matenda otseka matumbo** (onani tsamba 95). Anthu amadandaula kuti alodzedwa ndi mfiti kapena mizimu yoipa ndipo amayesayesa kuchiza matendawa potsata njira za matsenga.

Nthawi zina asing'anga amanamizira kuchotsa kanthu kabweya ndi minga poyamwa pamimba.

Matenda osiyanasiyana omwe amayambitsa kupweteka kwa m'mimba omwe nthawi zina amatchedwa matenda otseka ndi awa:

- kamwazi (onani tsamba 162)
- njoka zam'mimba (onani tsamba 146)
- kutupa kwa mimba chifukwa chochepa zakudya m'thupi (onani tsamba 117)
- kudzimbidwa chifukwa chakudya zosayenera (onani tsamba 131)
- kusagayika kwa chakudya kapena zilonda zam'mimba (onani tsamba 133)
- kudzimbidwa (onani tsamba 95)

Ambiri mwa matenda amenewa sangachizidwe potsata njira za matsenga. Ndi kofunika kupeza matenda enieni ndi kupeza njira zowachizira.

KUPWETEKA KWA CHIUNO Dzina la kudera la kwanu: _____


Ili ndi dzina loperekedwa pa kupweteka kulikonse kumene amayi amamva m'mimba mwawo. Nthawi zambiri ululu wotere umafikanso kumsana. Ululu wa wotere umayamba pa zifukwa zotere:

- vuto la m'ziwalo zochotsa mkodzo (impso, chikhodzodzo ndi mitsempha yomwe imalumikiza ziwalozi, onani tsamba 244)
- nthenda kapena zotupa mu chiberekero (tsamba 250) kapena pathupi posakhazikika m'malo mwake (onani tsamba 298)
- kupotokola kapena kupweteka chifukwa cha mpweya wa m'mimba (onani tsamba 162)
- kupweteka kwa nsonga yathumbo (onani tsamba 95)
- kupweteka pa nthawi ya msambo kapena kupita kumwedzi (onani tsamba 261)



KUPHWANYA KWA THUPI Dzina la kudera la kwanu: _____

Awa ndi matenda aliwonse adzidzidzi omwe amamuchititsa munthu kuti awoneke odwala kwambiri. Matenda otere angagwire:



Ena amanena kuti matenda amenewa amagwira anthu amene amadya zakudya **zoletsedwa** mwana akabadwa kapena chifukwa chakuti akumwa mankhwala ena ake kapena amene ali ndi chimfine kapena chifuwa. Kunena zowona **zakudya zoletsedwazo si kuti zimakhala ndi vuto lililonse** ndipo mwina ndi zakudya zomwe thupi likusowa.

Matenda osiyanasiyana amene nthawi zina amangotchedwa 'kuphwanya kwa thupi' amayamba pa zifukwa izi:

- Kudya poyizoni kudzera m'chakudya, kudya chakudya chowonongeka, kumayamba kusanza mwadzidzidzi kotsatizana ndi kupotokola m'mimba, komanso kufowoka (tsamba 140).
- Ziwengo mukadya zakudya zina (shelofish, chokoleti) kapena kumwa mankhwala ena Kapenanso kubayidwa jakisoni wa penesirini. Ziwengozi zitha kuyambitsa kusanza, kutsekula m'mimba, kutuluka chitungu kwambiri, kuvutika popuma, kumva kunyerenyesa komanso kuda nkhwala kwambiri (tsamba 175)
- Kupweteka kwa m'mimba kapena m'matumbo (tsamba 162), kutsekula m'mimba (tsamba 170), kusanza (tsamba 94).
- Kuvutika popuma: chifukwa cha mphumu (tsamba 176) chibayo kapena kutsamwa (tsamba 80).
- Matenda a kugwa (linjirinjiri kapena chifufu), (tsamba 188) kafumbata (tsamba 192), matenda oumitsa khosi (tsamba 195), poliyo (tsamba 333), kufa kwa ziwalo (tsamba 346).
- Matenda a mtima: makamaka anthu okalamba (tsamba 345).

NTHENDA YA MUTU WOBWEBWETETSA (HYSTERIA)

Dzina la kudera kwanu: _____

Nthendayi imayamba chifukwa cha mantha, ufiti, matsenga, kapena mizimu yoipa. Munthu wodwala nthendayi amakhala wa zinjenge komanso wamantha. Atha kukomoka, kunjenjemera, kuchita zinthu zosadziwika bwino, kusowa tulo, kuwonda ndiponso atha kumwalira.

Za matenda wa malinga ndi kufotokoza kwa makono:

1. Kwa anthu ambiri, nthenda ya mutu wobwebwetetsa ndi mantha chabe amene amayamba chifukwa cha mphamvu ya zikhulupiriro (onani tsamba 4). Mwachitsanzo; mayi amene akuwopa kuti munthu wina amulodza amachita zinjenge ndipo sadya ndi kugona mokwanira. Kenaka amayamba kufowoka ndi kuwonda. Akawona izi amawona ngati walodzedwa ndipo mantha ake amachulukira kotero matendawo amakulirakulira.
2. Kwa anthu achinyamata, matenda otere akhoza kukhala njira yothawira pa zinthu zomwe safuna kukumana nazo. Mwachitsanzo, msungwana wapasukulu amene watenga pathupi atha kukhala ndi mantha pa chidzudzulo cha makolo komanso kukhumudwa chifukwa chakusiya sukulu. Chifukwa cha maganizo otere, msungwanayo atha kukhala ngati akudwala matenda otere, nagwa ngati wakomoka nagonekedwa kuchipatala. Izi zikhoza kuchotsa mavuto ake enieniwo kwa kanthawi kochepea.
3. Zizindikiro za nthenda zina zitha kusokonezedwa ndi matendawa. Kwa ana aang'ono ngakhalenso okulirapo, maloto oyipa angathe kumuchitita mwanayo kuti azibwebweta kapena kudzuka ndi mantha. Kutentha thupi komwe kumayamba ndi matenda aliwonse kutha kuyambitsa kuti munthu aziyankhula zosadziwika bwino kapena kuonetsa chikhalidwe chachilendo (*delirium*). Nthawi zina zizindikiro za kafumbata (tsamba 192), nthenda youmitsa khosi (tsamba 195), kapena chiwewe (tsamba 191) zitha kuwoneka ngati zizindikiro za nthenda ya mutu wobwebwetetsa.

Chithandizo chake:

Pamene nthenda ya mutu wobwebwetetsa yayamba chifukwa cha nthenda ina yodziwika, chizani nthendayo. Thandizani kuti munthuyo kuti amvetse chomwe chayambitsa vutolo. Ngati ndi kofunika, dziwitsani anthu odziwa bwino ntchito zachipatala.

Pamene nthendayi yayamba chifukwa cha mantha, mutonthozeni ndipo muzindikiritsemi kuti vutolo ladza chifukwa cha mantha. Machiritso okhudza zamatsenga ndi machiritso ena apakhomo nthawi zina amathandiza.

Ngati munthu wodwalayo akupuma mofulumira ndi mwamphamvu, thupi lake litha kukhala kuti likulandira mpweya wambiri ndipo vutoli litha kuyambitsa nthendayi.

NTHENDA YA MUTU WOBWEBWETETSA WOYAMBA CHIFUKWA CHA MPWEYA WAMBIRI

Zizindikiro:

- munthu amakhala ndi mantha kwambiri
- kupuma mofulumira
- kuthamanga ndinso kugunda mwamhamvu kwa mtima
- kusamva bwino pankhope, m'manja, m'mapazi
- kukungana kwa mnofu

Chithandizo chake:

- Muthandizeni munthuyo kukhala chete.
- Muuzeni kuti azipumira mu thumba yapepala (pepabagi) pang'onopang'ono. Apume mpweya womwewo kwa mphindi ziwiri kapena zitatatu. Izi zingamuthandize kuti mtima ukhale pansu.
- Mufotokozereni kuti vuto lake si lowopsa ndipo kuti akhala bwino posachedwa.



Kusokoneza kodza chifukwa cha mayina

Tsamba lino lifotokoza za kusokoneza kodza pamene mayina monga khansa (*cancer*) ndi khate atanthauza chinthu chimodzi kwa madokotala pamene anthu a kumudzi ali ndi tanthauzo lawonso. Pokamba za madokotala komanso pogwiritsira ntchito bukuli:

Pewani kusamvetsa – tsatirani zizindikiro ndi mayambidwe a matendawo koma mosatsatira dzina lomwe anthuwo apereka.

KHANSA (CANCER) Dzina la kudera la kwanu: _____

Anthu ena akumudzi amati **'khansa'** ndi matenda aliwonse owopsa a pakhungu makamaka ngati pakhungu pali zilonda (tsamba 89) kapena payamba kuwola (chilonda cha njirda) (tsamba 224).

Pa mafotokozedwe amakono akuchipatala, khansa ndi chinthu chotupa (kapena kumera) pa chiwalo chilichonse chathupi. Mitundu ya khansa ndi iyi:

khansa ya pa khungu
(onani tsamba 223)



khansa ya m'mawere
(onani tsamba 297)



khansa yam'chiberekero
(onani tsamba 298)



Chinthu chilichonse chotupa **chosapweteka** chomwe chikumera pa thupi lanu chikhoza kukhala khansa. Khansa ndi yowopsa ndipo nthawi zambiri imafunika kuchita opaleshoni.

Ngati muwona zizindikiro za khansa kawonaneni ndi dokotala.

KHATE (LEPROSY) Dzina la kudera la kwanu: _____

Anthu ena akumudzi amaganiza kuti mawanga aliwonse owoneka kuti mbee pa khungu ndi **'khate'**. Kusokoneza kotere kumadza pa zifukwa izi:

- matenda a pakhungu onyerenyesa (onani tsamba 218)
- *impetigo* (mabala a pakhungu opatsirana, onani tsamba 214)
- mabala akale omwe amapola ndi zipsera zoyererako
- *Tinea Versicolor* (zikanga za m'thupi ndi kumaso, onani tsamba 218) Mpovuta kuti musiyanyitse. Muuzeni mlangizi wazaumoyo.

Anthu omwe adaphunzira za chipatala ndi amene angadziwe za nthenda ya khate (onani tsamba 199).



Mwana uyu ali ndi matenda apakhungu osati a khate

Kusokoneza kwa pakati pa matenda otenhethsa thupi

KUTENTHA KWA THUPI Dzina la kudera la kwanu: _____

Tikanena kuti 'kutentha kwa thupi' tanthauzo lake ndiye kuti **thupi latentha mopyola muyezo kusiyanana ndi momwe thupilo limayenera kutenthera**. Pali matenda ena angapo owopsa ndithu omwe amatenthetsa thupi omwe anthu amangot 'kutentha kwa thupi'.



Pofuna kuchiza kapena kupewa matenda otere ndi bwino kudziwa momwe tingawasiyanitsire.


Nawa matenda ena amene amatenthetsa thupi. Zithunzi zojambulidwazi zikusonyeza **kutentha ndi kuzizira kwa thupi** monga zimakhallira pa nthenda iliyonse.

Malungo: (onani tsamba 181)

Poyamba mutha kufowoka, kuzizidwa ndi kuyamba kunjenjemera pamene thupi likutentha. Kutenthedwa ndi kuzizidwa kutha kupitirira kwa masiku angapo ngati odwalayo sapatsidwa mankhwala. Munthu amatuluka thukuta pamene thupi lake likuzizira ndipo amanjenjemera pamene thupi likutenthanso. Kamodzikamodzi malungo amatenthetsa thupi pakatha masiku awiri kapena atatu aliwonse amene munthuyo akudwala. Pa masiku ena apakatiwo, amawoneka ngati wachira.

MALUNGO — MOMWE THUPI LIMATENTHERA

Mzerevo ukusonyeza kutentha ndi kuzizira kwa thupi.




Taifodi: (onani tsamba 196)

Nthendayi imayamba ngati chimfine. Thupi limapitiriza kutentha tsiku ndi tsiku ndipo mtima umagunda pang'onopang'ono. Nthawi zina wodwala amatsekula m'mimba ndipo thupi limasowa madzi komanso amanjenjemera komanso kubwebweta. Munthu amadwala kwambiri

TAIFODI — MOMWE THUPI LIMATENTHERA

Thupi limanka litentha tsiku ndi tsiku.



Taifasi (Typhus): (onani tsamba 198)


Nthendayi imafanana ndi taifodi. Pakhungu pamachita tizilonda ngati chikuku.

Nthenda yam'chiwindi (Hepatitis): (onani masamba 183 ndi 204)

Munthu wodwala sakhala ndi chilakolako chofuna chakudya, ndipo safunanso kusuta. Amafuna kusanza ndipo maso ndi khungu lake limasanduka chikasu, mkodzo nawonso umakhala wachikasu (orange) kapena wodera mofiirira (brown). Chimbudzi chake chimakhala chotuwa. Nthawi zina chiwindi chimatupa ndi kufewa. Pambuyo pake thupi limatentha pang'ono ndipo wodwala amafowoka

NTHENDA YAM'CHIWINDI — MOMWE THUPI LIMATENTHERA


Thupi limatentha pang'ono.



Chibayo: (onani tsamba 180)

Wodwala amapuma mofulumira koma mosalowa m'kati. Thupi limatentha mwamsanga. Amatsokomola ndipo makhololo amakhala obiriwira, achikasu kapena amagazi, m'chifuwa mumapweteka ndipo munthu amadwala kwambiri.


CHIBAYO — MOMWE WODWALA AMATENTHERA THUPI



Kutentha thupi kwa nyamakazi (Rheumatic fever): (onani tsamba 329)

Nthendayi imagwira kwambiri ana ndi achinyamata (*joint pains*). M'maluma a mafupa mumapweteka. Thupi limatentha kwambiri. Kawirikawiri nthendayi imayamba pambuyo podwala zilonda zakukhosi. M'chifuwa mumapweteka komanso kupuma wopereweza ndipo manja ndi miyendo zimanjenjemera kapena kusuntha mosaletseka..

MATENTHEDWE ATHUPI ANTHENDAYA KUTENTHA THUPI JWANYAMAKAZI




Kutentha thupi kosinthisantha Brucellosis: (onani tsamba 196)

Poyamba wodwala amatopa ndipo mutu umapweteka komanso amamva kupweteka m'mafupa. Thupi limatentha komanso kutuluka thukuta pa nthawi ya usiku. Kutentha thupi kumasiya kwa masiku ochepa kenaka ndikuyambiranso. Zimenezi zimachitika kwa miyezi ingapo ngakhalenso zaka.

MATENTHEDWE ATHUPI A NTHENDA YA BRUCELLOSIS


Kutentha thupi kumabwera masana ndi kupita usiku



Vingwangwa kapena kaliwawa mwana akangobadwa (childbirth fever): (onani tsamba 294)

Amayamba pambuyo pa tsiku limodzi kapena masiku angapo pamene mayi wabereka mwana. Poyamba thupi limatentha pang'ono kenaka limatentha kwambiri. Kumaliseche kwa wodwala kumatuluka zamadzimidzi zonunkha ndipo nthawi zina magazi.

MATENTHEDWE A THUPI A VINGWANGWA



Matenda onsewa ndi owopsa. Kuwonjezera pa matendawa, palonso matenda angapo amene amatenthesa thupi kotero amavuta kusiyaniitsa. Ngati ndi kothekeka pitani kuchipatala.